

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

AMBUYE, TIPHUNZITSENI KUPEMPHERA

(Mu nkhani iyi, Pemphero la Ambuye latengedwa kuchokera pa Mateyu 6:9-13).

Pa Luka 11, ophunzira anabwera kwa Khristu namupempha kuti: “Ambuye, tiphunzitseni ife kupemphera.” Pemphero lalikulu limene linalembedwa limadziwika kuti “Pemphero la Ambuye” ndipo ndi ndondomeko ya pemphero yakuti titsatire. Uwu ndi ndalitsa wodabwitsa koposa popeza tikuphunzira za m'mene tingapempherere kuchokera kwa mwana wa Mulungu mwiniwake. Mu ndondomeko iyi ya pemphero muli magawo ambiri amene akhoza kuthandiza anthu kuti apemphere mwamphamvu pamene akutsekula mitima yao moona mtima ndi mwachikondi, nadzikhuthula ndikupereka zopempha zao kwa Mulungu. “Chifukwa chake pempherani inu chomwechi...”

“Atate athu” — Ubale wa umunthu. Chiyambi cha pempheroli chikuonetsa chitsanzo cha ubale wokongola umene ulipo pakati pa Mulungu ndi anthu. Chikulongosola kulimbika mtima kumene tili nako mwa Mulungu ngati atate athu komanso chikondi chimene tili nacho pokhala ana ake. Ife ndife ana opezedwa a Mfumuyo. “Athu” ndi mau owonetsa kuti tilipo ambiri ndipo akuonetsa umodzi ndi kuvomereza kumene Mulungu ali nako, popeza iye ali Atate wa ana enanso amene ali abale ndi alongo athu mu uzimu.

“Wa Kumwamba,” — Chikhulupiriro/Kuvomereza. Chidziwitso chokhazikika ndi chitsimikizo chakuti Mulungu aliponsepose komanso ndi wamphamvuzonse. Tikhulupirira mwa Iye ndipo timdziwa amene tikumpempherera.

“Dzina lanu liyeretsedwe.” — Kulemekeza/Kumukweza/Kulambira. Kuyeretsedwa kutanthauza kupatulidwa, kuikidwa padera chifukwa cha ntchito ina yake. Pemphero ndi nthawi yolemekeza ndi yopereka ulemu kwa Mulungu ndiponso kuvomereza ndi mitima yathu, maganizo athu komanso mau athu kuti Iyeyo ali woyera ndi wokhala kumwamba ndipo alamulira miyoyo yathu. Pemphero siliyamba ndi kupempha koma ndi kulambira dzina loyera la Mulungu.

“Ufumu wanu udze.” — Kudikira/Kuyembekezera.

Kumeneku ndiko kumupempha Mulungu mwachiyembekezo kuti Iye atitsogolere ndipo akhale nafe. Ndiko kuyembekeza ulamuliro wathunthu wa Mulungu pa miyoyo yathu komanso kuti mphamvu za Satana ziwonongedwe. “Pakuti ufumu wa Mulungu sukhalachakudya ndi chakumwa, koma chilungamo, ndi mtendere, ndi chimwemwe mwa Mzimu Woyera.” (Aroma 14:17). Ufumu wa Khristu ndiwo ufumu wa uzimu umene umakhala mkati mwa munthu.

“Kufuna kwanu kuchitidwe, monga Kumwamba chomwecho panso pano.” — Kugonjera/Kudzikhuthula.

Chifuniro cha Mulungu chili chathunthu kumwamba koma chimachitika mwa ife pamene tigonjera matupi athuwa pamodzi ndi chifuniro komanso zokhumba zake m'manja a Mulungu. Monga m'mene Yesu anapempherera m'Getsemane kuti, “si monga ndifuna Ine, koma Inu.” Limeneli ndi gawo la pemphero kumene kuli kugonjera kuzonse zimene tili nazo kuti zikhale zakezake za Mulungu.

“Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero.” — Kupempha/Kufunsa.

Titatha kulambira ndi kudzikhuthula, timakhala pa nthawi yakuti tikhoza kumupempha Mulungu zosowa za moyo. Timupemphe Mulungu zinthu zonse zokhudza moyo ndi umulungu kuti potero tikakhoze kukwaniritsa chifuniro chake m'miyoyo yathu. Chimenechi chimakhudza osati buledi wathupi yekha komanso zisomo zauzimu zimene zimafunika kutithandiza ife kuti tikule ndi kukhwima mu chifooko chathu.

“Ndipo mutikhululukire ife zochimwa zathu.” — Kulapa/kupembedzera.

Ifeyo sityenera kuti Mulungu atikhululukire, komabe Iye ali wofuna ndi wokonzeka kuti atikhululukire osati machimo athu

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Pemphero lalikulu limene linalembedwa limadziwika kuti “Pemphero la Ambuye” ndipo ndi ndondomeko ya pemphero yakuti titsatire.”

Mau a Mkonzi

Kalozera posanthula
Baibulo: Pemphero

Chiphunzitso cha
Pemphero

Funso Yankho

Kodi Mukudziwa?

Pemphero La Yabezi

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

okha komanso zofooka ndi zolephera zathu. Nkoyenera kuti tidzifufuze tokha modzichepetsa ndi kuvomereza kulephera kwathu kuuzimu. Pemphero la kulapa likhoza kupemphereredwa pagulu, monga m'mene Daniele anachitira popembezera Israele pofunsa chikhululukiro cha Mulungu.

“Monga ifenso takhululukira amangawa athu.”—Kuchita chifundo/Kukhululukira. Mulungu ali wokonzeka kutikhululukira ife monga ife tawachitira chifundo ndi kuwakhululukira iwo amene atichimwira. Kufunafuna thandizo la Mulungu mu ubale wathu ndi anthu ena ndi koyenera pa ubale wathu ndi Mulungu.

“Pemphero lili
ngati chingwe

chotilumikizitsa ife ndi

Mulungu. Liri gawo

lofunikira pa moyo

wathu wachikhristu.”

“Ndipo musatitengere kokatiyesa,”—Chitsogozo. Mayesero komanso zoopsa zauzimu ndi zenizeni ndithu. Ngati titsatira chitsogozo cha Mulungu, inde tidzayesedwa, koma sitidzagonjera ku yeserolo mpaka kuchimwa. Kufunafuna ndi kumvera chitsogozo cha Mulungu zidzatipangitsa kuti ife tipewe mavuto ochuluka.

“Koma mutipulumutse kwa woipayo:”—Chitetezo/Kudalira.

Mphamvu zogonjetsera sizili mu nyonga zathu koma mu mphamvu ya Mulungu. Iye adzatiteteza ife ku machenjerero ndi misampha ya mdaniyo ngati tidalira chithandizo chake.

“Pakuti wanu ndi ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemero,”—

Kuvomereza. Ife tili ofooka ndipo sitikwanitsa koma mwa Khristu ndife amphamvu ndipo tikhoza kukhala moyo wovomerezeka pamaso pa Mulungu. Mphamvu ndi ulemmerero wonse zikhala pa Mulungu mwiniwake, osatinso munthu wina, popeza Iye ndiye wopereka zinthu zonse zabwino. Pemphero limayamba ndi kumalizitsa chikhulupiriro, kudzichepetsa, kulemekeza ndiponso kumulambira Mlengi.

“Ku nthawi za nthawi.”—Nthawi zopanda malire. Ufumu wa Mulungu, chifundo ndi chikondi chake, nzosatha ndipo nzamuyaya.

“Amen.”—Chitsimikizo. Zikhale momwemo. Zitero basi.

Pemphero ndi lofunikira pa ubale wathu ndi Mulungu. Yesu anapereka nondomeko ya m'mene tingapempherere kwa mphindi yosakwana imodzi popemphera kwa Atate. Lili lalifupi ndi lochepa koma kumakhala kudzipereka ndi mtima wa chikondi komanso kulambira pomwe timupempha Mulungu pa zofuna za moyo wathu. Pemphero ili lamphamvu likusiyana kutalitali ndi mapemphero ena onena zinthu zosamveka komanso odzikuzwa amene amapemphereredwa m'nyumba zambiri za Akhristu komanso m'mpingo pa dziko lonse. Pemphero lili ngati chingwe chotilumikizitsa ife ndi Mulungu. Liri gawo lofunikira pa moyo wathu wachikhristu. Pempheroli likhoza kupemphereredwa monga lalembedwera pamene tikulinena kuchokera pansu pa mtima, kapena magawo ena a pempheroli akhoza kuikidwa mu mapemphero athu a tsiku ndi tsiku amene timapemphera kwa Atate wathu wakumwamba. Ambuye, tiphunzitseni kupemphera ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Musadere nkhawa konse; komatu m'zonse ndi pemphero, ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. —Afilipi 4:6

Tipemphere kwa Ambuye. Pemphero limasintha zinthu. Pempheranibe mpaka yankho lanu litabwera. Pemphero ndi makiyi. Pemphero ndi chipolopolo. Nyimbo izi ndi mau awa zakhala zikuzungulira mumtima mwanga pomwe ndakhala ndikulingalira za mutu wa ulendo uno umene uli: pemphero.

Pemphero limaoneka ngati lowawa kwa Akhristu ena ndipo ndi chinthu chimene timadzimvera chisoni popeza sitililabadira kwambiri. Tilole Mzimu wa Mulungu atithandize kumvetsetsa kuti pemphero lili mwai wapaderadera wakuti tikhale ndi danga lalikulu lakuti tikonzedwe mwachikondi ndi Mzimu wa Mulungu. Imeneyi ndi nthawi yolambira Mulungu komanso yotula nkhawa zathu pa Ambuye. Tili ndi mdalitso wakuti tikhoza kupereka nkhawa za mumtima mwathu kwa Mulungu amene amatikonda ndipo ali wokonzeka kutithandizira kunyamula katundu wathu.

Muli mphamvu yaikulu mu pemphero maka pamene tifika kwa Mulungu mwa chikhulupiriro. Ineineyo ndikhoza kuchitira umboni kuti ndaonapo zodabwitsa za machiritso, ndatulutsako ziwanda ndapeza mtendere pa nthawi ya masautso ochulukana ndi zina zambiri kudzera mumphamvu ya pemphero. Ndapempheranso pamene zinthu zimaoneka ngati palibe chikusintha; koma nthawi ngati imeneyo ndi pomwe chikhulupiriro chathu chikuyenera kuzikika pa nzeru za Mulungu osati mu yankho la pemphero lathulo. Kupemphera kumatisintha ifeyo, popeza kumatiika pamalo amene tikhoza kumudalira Mulungu. Pamene ndi pomwe Mulungu akhoza kugwira bwino ntchito, popeza mphamvu ya pemphero sili mu zomwe ife tingachite, koma zomwe Mulungu amachita mwa ife mwa ubwino ndi chifundo chake.

Pemphero si kungotsatira m'ndandanda wa malamulo a zimene tikuyenera kunena kapena njira yabwino yakuti tinene momveka bwino zimene tikufuna. Pemphero limapyola pa chiphunzitsa kukafika pa zokhumba za munthu komanso kuyanjana kwathu ndi Ambuye Mpulumutsi wathu. Ndikukhulupirira kuti sitichedwetsedwa ndi chiphunzitsa chimenechi. Ngakhale kuti chiphunzitsa chili chofunika, komabe chofunikira ndiko kuona mdalitso wa pemphero. Pamene ndimawerenga komanso kuchita kafukufuku, ndinadabwa kuti pali malemba ochulukana amene akunena za pemphero. Kalata uyu akungonena mwa apo ndi apo zimene Baibulo limaphunzitsa ndipo sitinanene zonse. Pemphero langa ndilo lakuti owerenga aliyense afulumizidwe kuti pafupipafupi adzipeza malo achete amene akhoza kukhala ndi Ambuye mu pemphero. Mupeza kuti izi zidzakulimbikitsani kukula mu uzimu komanso lidzakhala yankho kuzinthu zambiri zimene anthu amalimbana nazo, mavuto a m'banja, zosautsa za m'mipingo ndi zina zotere. Mwachisomo cha Mulungu, mudzapeza kuti pemphero limakusinthani. Tiyeni tidzipemphera ndi chiyembekezo.

Michael W. Smith

January 2020

Kupemphera pa Nthawi ya chakudya



Kangapo konse timawerenga mu Malemba za kuti Khristu anapemphera asanayambe kudya. “Ndipo m'mene anayang'ana kumwamba, anadalitsa, nanyema, napatsa mikateyo kwa ophunzira.” (Mateyu 14:19). Mu ndime zosiyanasiyana, wolemba mabuku a uthenga wabwino nthawi zina anagwiritsa ntchito mau akuti “anadalitsa” pamene ena anagwiritsa ntchito mau akuti “anayamika.” Nzosangalatsa kuona kuti Khristu kwambiri amatsatira chikhalidwe chiChiyuda osati chodalitsa buledi koma kuyamika kwa Mulungu. Ayuda analetsedwa kuti asamadye ndi kumwa asanayambe kuvomereza Mulungu poyamika.

Mdalitso waChiyuda unali motere: “Wodalitsika ndinu Ambuye, Mulungu wathu, Mfumu ya chilengedwe chonse, amene mumatipatsa mkate kuchoka kunthaka!”

Mwambo ndi mchitidwe wa nthawi imeneyo unali wa “kudalitsa” chakudya komanso kuyamika kapena kupereka madalitso kwa Mulungu amene amapereka chakudyacho. Paulo “anatenga mkate, nayamika Mulungu pamaso pa onse; ndipo m'mene adaunyema anayamba kudya” (Machitidwe 27:35).

Ndi mwambo woyenera kuwutsatira pothokoza kwa Mulungu chifukwa cha zimene watipatsa panthawi iliyonse imene tili pachakudya, kaya ndi pagulu kapena patokha.

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Pemphero

Kuwerenga Malemba: Pempherani kosalekeza. —1 Atesalonika 5:17

Tanthauzo: Pemphero ndiko kulankhulana ndi kulumikizana ndi Mulungu. Mu pemphero muli zinthu izi “kulemekeza, kapena kuonetsa kuti tikuzindikira kuti Mulungu ndi waulemereo ndi wangwiro, kulapa machimo athu, kupempherera chifundo ndi chikhululukiro, kupembedzera madalitso pa anthu ena, ndi kuthokoza” [Webster’s Dictionary, 1828].

Mwachidule: Pemphero ndi chinthu chofunikira ndipo kudzera mwa ilo anthu akhoza kumudziwitsitsa Mulungu komanso kuyanjanana naye. Pemphero ndi njira yolambira ndi kukweza Mulungu. Pemphero ndi mseu umene munthu akhoza kudzeramo kuti apeze chipulumutso ndi zisomo za Mzimu Woyera. Pemphero ndi chingwe chimene chimakafika kumwamba kuchokera panso pano ndipo limamuthandiza munthu kuti adziwe ndi kumvetsetsa chifuniro cha Mulungu. Pemphero limasintha mtima ndipo mwa chikhulupiriro likhoza kusintha nyengo kudzera mu mphamvu ya Mulungu. Pemphero ndi chimodzi mwa zinthu zofunikira kwambiri pofuna kuti munthu akhale ndi moyo wachikhristu wopambana.



I. Pemphero lilamulidwa

- A. “Ayenera iwo kupemphera nthawi zonse.” Luka 18:1
- B. “Chitani khama m’kupemphera.” Akolose 4:2
- C. Pemphani, Funafunani, gogodani. Luka 11:9-10

II. Cholinga/Phindu/Mphamvu ya pemphero

- A. Ubale/Chiyanjano. Genesis 5:24, Yereimiya 29:11-13, Yohane 15:5.
- B. Kupembedza. Salmo 103:1.
- C. Chipulumutso. Machitidwe 2:21.
- D. Machiritso. Yakobo 5:13-16.
- E. Chisomo/Mphamvu. Ahebri 4:16.
- F. Nzeru. Yakobo 1:5.
- G. Kutula nkhawa. 1 Petro 5:6-7, Salmo 107:28-30.
- H. Mphamvu ya kugonjetsa. Mateyu 26:41.

III. Tipemphere motani

- A. Mu dzina la Yesu. Yohane 16:23.
- B. Mwachikhulupiriro. Ahebri 11:6.
- C. Modzichepetsa. Yakobo 4:6.
- D. Mu Mzimu. Yuda 1:20.
- E. Moyamika. Afilipi 4:6.
- F. Osabwerezabwereza mau. Mateyu 6:7-8.

IV. Kodi Mulungu amamva ndi kuyankha pemphero la ndani?

- A. Odzichepetsa/Olapa. 2 Mbiri 7:14.
- B. Iwo ofuna kumasulidwa. Yowele 2:32, Salmo 86:7.
- C. Olungama ndi omvera. Yakobo 5:16, 1 Petro 3:12, 1 Yohane 3:22.
- D. Iwo okhulupirira. Ahebri 11:6, Marko 11:24.
- E. Molingana ndi chifuniro chake. 1 Yohane 5:14-15.
- F. Kupembedzera motsogozedwa ndi Mzimu. Aroma 8:26-27.

V. Tipempherere ndani

- A. Ife eni. Masalmo 55:16, 2 Akorinto 12:8-10.

- B. Oyera mtima/Atumiki. 1 Atesalonika 1:2, Aefeso 6:18-19, 2 Atesalonika 3:1.
- C. Ogwira ntchito yotuta dzinthu. Luka 10:2.
- D. Osapulumsidwa. Aroma 10:1.
- E. Adani. Mateyu 5:44.
- F. Maiko/Olamulira. 1 Timoteo 2:1-3.

VI. Zimene zimaletsa pemphero

- A. Uchimo. Miyambo 15:29, Yohane 9:31.
- B. Malingaliro olakwika. Yakobo 4:3.
- C. Kusakhululuka. Marko 11:25-26.
- D. Kudzilungamitsa. Luka 18:9-14.
- E. Mavuto a banja. 1 Petro 3:7.

VII. Tipemphere patipo

- A. Patokha. Mateyu 6:5-6, Mateyu 14:23.
- B. Pagulu. Machitidwe 4:31, Machitidwe 12:5,12.

VIII. Malonjezo kwa iwo amene amapemphera

- A. “Chidzapatsidwa kwa inu.” Mateyu 7:7-8
- B. “Ngati awiri a inu avomerezana.” Mateyu 18:19
- C. “Pemphani chilichonse chimene mufuna.” Yohane 15:7

Kumaliza

Koma chitsiriziro cha zinthu zonse chili pafupi; chifukwa chake khalani anzeru, ndipo dikirani m’mapemphero. —1 Petro 4:7

MITUNDU YA PEMPHERO

KUKWEZA

KULEMEKEZA MULUNGU

KUDZIKHUTHULA

KUPEMPHA CHIKHULULUKIRO KWA MULUNGU

MAPEMPHO

KUPEMPHA KUTI MULUNGU ATIKONDERE

KUPEMBEDZERA

KUPEMPHERA M'MALO MWA ANTHU ENA

KUYAMIKA

KUTHOKOZA MULUNGU


Chiphunzitsa cha Pemphero

KUITANIDWA KUTI TIYANJANE NDI MLENGI WATHU

Pemphero ndi chitsanzo cha ubale umene tilinao ndi Mulungu. Ndi chinthu chodabwitsa kufika pamaso pa Mulungu ndi kuyanjana naye panthawi iliyonse, pena paliponse komanso m'nyengo iliyonse. Pemphero sinthawi yongofunsa chinthu, koma ndi nthawi yolambira ndi kudzikonzanso kuuzimu.

Linalamulidwa ndi Khristu

Yesu analamulira kuti “ayenera iwo kupemphera nthawi zonse, osafooka mtima” (Luka 18:1). Chimenechi chikubwerezedwa m'malemba kuti: “Chitani khama m'kupemphera, nimudikire momwemo” (Akolose 4:2). Chokhumba cha Mulungu ndichakuti munthu akhale naye pa ubale weniweni komanso wapamtima. Ubale



“Pemphero ndi gawo lalikulu ndi lofunikira kuti ifeyo tikhalebe mwa Khristu, ndi kutenga nao chikhalidwe chake komanso kubala chipatso chauzimu.”

wopindulitsa chotere umatenga nthawi ndiponso umafunika kuwutengulira, ndipo pemphero ndilo njirayo imene anthu akhoza kulumikizana ndi Mulungu. Popanda kulumikizana, sitinganene kuti pali ubale. Mulungu amafuna kuti ifeyo tidziyenda naye tsiku ndi tsiku monga momwe anachitira Enoki. Yesu anapempha ophunzira ake kuti akhalebe mwa Iye monga nthambi imene yalumikizidwa kumpesa. Pemphero ndi gawo lalikulu ndi lofunikira kuti ifeyo tikhalebe mwa Khristu, ndi kutengera chikhalidwe chake komanso kubala chipatso chauzimu. Pa Yakobo 4:8 akuti, “Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu.”

Kupembedza koono ndi kwa pansi pamtima

Pemphero lenileni limaposa mau ongoloweza pamtima. Pemphero

ndiko kufunafuna Mulungu mwakhama kuchokera mu mtima umene uli wofunitsitsa kumukhudza Mpulumutsiyo. “Mudzanka ndi kupemphera kwa Ine, ndipo ndidzakumverani inu. Mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna ndi mtima wanu wonse” (Yeremiya 29:12-13). Pemphero ndi nthawi yopembedza Ambuye ndi kukweza dzina lake. Pemphero lotere limaika mtima ndi maganizo pamalo akuti akhoza kulandira kuchokera kwa Mulungu komanso zimabweretsa moyo womvera.

Makiyi otsegulira makomo

Phindu ndi mphamvu ya pemphero sikuyenera kuchepetsedwa, popeza pemphero lenileni ndiwo makiyi otsegulira makomo ambiri. Pemphero

lamumtima ndi limene limabweretsa chipulumutso kumtima. “Yense amene akaitana pa dzina la Ambuye adzapulumutsidwa” (Machitidwe 2:21). Ndi pemphero, lomupempha Mulungu pampando wake wachifumu kuti mwaumulungu wake alowererepo pa zochitika za nthawi zonse, limene limabweretsa machiritso kwa odwala. “Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akulu a Mpingo, ndipo apemphere pa iye...ndipo pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa” (Yakobo 5:14-15). Pemphero linasintha zinthu nthawi zambirimbiri m'Malemba ndipo likuchitanso chimodzimidzi kwa anthu a Mulungu a mu m'badwo uno.

Bwerani kwa Ine

Mu nthawi za mavuto, nkhwana ndi zosautsa za moyo, Mulungu akutiitana kuti tifike molimbika “poyandikira mpando wachifumu wachisomo, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa” (Aheberi 4:16). Ndi pemphero lokhalo limene lili lochokera pansi pamtima ndi lodzipereka kwa Ambuye kuti chisomo chake chifikire pamtima wofunitsitsa lomwe Ambuye amalilandira. Nthawi zambiri timataya mtendere ndi chimwemwe chifukwa anthu amakanika kuti akhale ndi nthawi yakuti apemphere. Pemphero ndi malo operekerana nkhwana zathu pa Mpulumutsi ndi kupeza mpumulo (1 Petro 5:6-7). Ndipo Salmo 107:28-30 likupereka chithunzithunzi chokongola cha nkhanayi yakuti: “Pamenepo afuulira kwa Yehova m'kusauka kwao, ndipo awatulutsa m'kupsinjika kwao. Asanduliza namondwe akhale bata, kotero kuti mafunde ake atonthole. Pamenepo akondwera, popeza pagwa bata; ndipo Iye awatsogolera kudooko afunako.”

Kulankhulana kwa mbali zonse ziwiri

Pemphero si kulankhula kwa mbali imodzi ayi, koma ndi nthawi yakukhala chete pamaso pa Mulungu pomwe mtima umvetsera kwa Mzimu molingalira. Malo awa a pemphero amamuthandiza mkhristu kuti akhoza kuliyaamba tsiku ndiponso kulowamo ndi mphamvu zochokera kwa Mulungu. Ngakhale kafukufuku wa maphunziro a zachikunja amaonetsa kuti kupemphera kumachepetsa kusinkhasinkha ndi nkhwana ndipo kumathandiza kuti munthu uone zinthu mwaubwino.

Pemphero ndi mwai wakuti tifunefune Mulungu kuti atitsogolere ndi kutipatsa nzeru (Yakobo 1:5). Nkofunikira “Chezerani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa”

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

(Mateyu 26:41). Pemphero ndi gwero la mphamvu zogonjetsera misampha ndi makhwekhwe a mdaniyo.

Mungapemphere motani

Baibulo limaphunzitsa mwa lamulo ndi mwa chitsanzo za m'mene tingapempherere. Akhristu akuyenera kupemphera mu dzina la Yesu (Yohane 16:23). Muli mphamvu mu dzina la Yesu ndipo tigwiritse ntchito dzinalo komanso ndi mphamvu yake. Anthu akuyenera kufunafuna Mulungu mwa chikhulupiriro popeza Mulunguyo “ali wobwezera mphotho iwo akumfuna

Iye.” (Ahebri 11:6). Pemphero lovomerezeka limakhala ndi kudzichepetsa kwa moyo ndi mzimu (Yakobo 4:6) ndipo libile kudzikuzana ndi kudziyenereza. Zopempha zathu kwa Ambuye zidziphatikizana ndi chiyamiko (Afilipi 4:6) ndiponso kuthokoza. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera mosachulutsa mau ndi kuti “musabwerezebwereze chabe” (Mateyu 6:7-8). Mulungu amadziwa chosowa chathu ngakhale tisanachitchule nkomwe mu pemphero. Mapemphero asamanenedwe ndi cholinga chofuna kuti ena akugomereni kapena kungodzionetsera koma kuti tilumikizane ndi Mulungu mu Mzimu. Ha! Onani mdalitso omwe ulipo podziwa kuti pomwe mau ndi maganizo sangabwere polemedwa mu Mzimu ndi kuperewera kwathu pamaso pa Mulungu, pamene Mzimu wa Ambuye

“Ha! Onani mdalitso omwe ulipo podziwa kuti pomwe mau ndi maganizo sangabwere polemedwa mu Mzimu ndi kuperewera kwathu pamaso pa Mulungu, pamene Mzimu wa Ambuye ‘apempherera oyera mtima monga mwa chifuno cha Mulungu.’”

“apempherera oyera mtima monga mwa chifuno cha Mulungu” (Aroma 8:26-27).

Amene Mulungu amamumvera

Malemba amanena momveka bwino pamalo angapo kuti Mulungu amatchera khutu ndipo amayankha pemphero pokhapokha ngati titakwaniritsa zinthu zina. Iye amayankha pemphero la moyo umene uli wodzichepetsa ndi wolapa (2 Mbiri 7:14). Iye amayankha pemphero la iwo amene aitanira pa Iye pofuna kuti apulumutsidwe (Yoweli 2:32). “Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m'machitidwe ake” (Yakobo 5:16). Mulungu amalemekeza mapemphero a oyera mtima ndi omwe amasunga malamulo ake (1 Yohane 3:22). Iye amasunthika pampando wake wachifumu ndipo zinthu zimasintha pamene pemphero liperekedwa mwa chikhulupiriro (Marko 11:24) ndi kumupempha Iye molingana ndi chifuniro chake cha umulungu (1 Yohane 5:14-15).

Mapemphero amphamvu

Palinso nyengo zina zimene zimaletsa kuti mphamvu ya pemphero isaonekere. Pa Yohane 9:31 akuti, “Tidziwa kuti Mulungu samvera ochimwa” ndipo pa Miyambo 15:29 akuti: “Yehova atalikira oipa; koma pemphero la

olungama alimvera.” Mulungu ndi wamphamvu zonse komabe sadzayankha pempho lililonse, makamaka pamene anthu apempha molakwika pofuna chinthu chimene akachigwiritsa kuti akwaniritse zokhumba zao zoipa (Yakobo 4:3). Mzimu wa kusakhululuka (Marko 11:25-26) kapena kudziyenereza (Luka 18:9-14) umaletsanso mapemphero. Mavuto a m'banja komanso kusowa kwa chisomo m'nyumba zimatchinga mphamvu ya pemphero. “Amuna inu...ndi kuchitira mkazi ulemu...kuti mapemphero anu angaletsedwe” (1 Petro 3:7).

Mitundu ya pemphero

Pali anthu ambiri ndipo pali zinthu zambiri zimene Baibulo limatiphunzitsa kuti tizipempherere. Titatha kulambira ndi kuyamika mu pemphero, nkofunikira kudzipempherera tokha—kuti tikule m'moyo wathu wauzimu ndi wathupi, komanso chifukwa cha zosowa za m'maganizo mwathu komanso zimene tikuzifuna kwa nthawi yochepa. Pemphero la banja, la zosowa za ena, la iwo amene sanapulumsidwe, la adani, la oyera mtima, la atumiki a Mulungu, kuti Ambuye atumize antchito ake, ndiponso maiko ndi olamulira - zonsezi zili zogwirizana ndi Malemba komanso cholinga cha pemphero.

Pemphero la patokha ndi la pagulu

Pali nthawi za pemphero la patokha ndi pemphero la pagulu monga ananenera mu Baibulo. Yesu mwiniwake anafuna gwero la mphamvu zimenezo kuchokera kwa Atate ndipo anachoka kangapo napita kukapemphera payekha. Pali nyengo zambiri pamene tikumva kuti anthu a Mulungu amapemphera pamodzi, ndipo amapembedzera limodzi pa chosowa chao kwa Atate. Pali mphamvu mu pemphero la umodzi ndipo limakwera kumwamba kumpando wachifumu wa Mulungu ngati nsembe yonunkhira. Pemphero lapatokha ndi nthawi yakuti tikhuthule zosowa zathu zonse pamaso pa Mulungu. Mu pemphero la pagulu, tikuyenera kulemekeza omvera mu zimene tikunena komanso mu kutalika kwa pempherolo.

Tipemphere nthawi yanji

Malingana ndi mbiri yakale, Ayuda anali ndi nyengo ziwiri za pemphero, m'mawa ndi usiku, ndipo ena amaonjezapo nyengo yachitatu ya masana dzuwa lili pa liwombo. Daniele anapemphera katatu pa tsiku (Daniel 6:10). Chipangano Chatsopano sichilamulira nthawi yeniyeni yakuti munthu adzipemphera koma chimaphunzitsa kuti “Pempherani kosalekeza” (1 Atesalonika 5:17). Mwana wa Mulungu akhale ndi mzimu wongofunabe kupemphera. Nkofunikiranso kuika padera nthawi yokhazikika yopemphera ndi kufunafuna Ambuye. Nthawi yabwino ingakhaleenso yotani koposa m'mawa musanayambe zochitika za tsikulo ndiponso usiku pamene mukumaliza tsiku. Uzimu wathu udzaumbidwa ndi nthawi zochulukira zopemphera ndi zokhala pamaso pa Ambuye.

Khalani tcheru ndipo pempherani

Pemphero ndiko kulumikizana ndi Mulungu ndipo nthawi zambiri limatengera kwambiri kusintha kwa maganizo ndi mzimu wathu kusiyana ndi kulandira yankho la kanthawi kochepe kuchokera kwa Mulungu. Pali mphamvu ndi phindu lalikulu mu pemphero. Monga mwa mau a mtumwi Petro, “Chitsiriziro cha zinthu zonse chili la pafupi; chifukwa chake khalani anzeru, ndipo dikirani m'mapemphero.” ■



Kodi ndi njira itiyi imene tikhoza kumagwiritsa ntchito popemphera?

Palibe njira yeniyeni yolondola imene munthu akhoza kugwiritsa ntchito pamene akupemphera. Pakati pa Ayuda Yesu asanabwere, njira yodziwika bwino popemphera inali yoimirira. Zikuoneka kuti Hana anaimirira pamene anali kupempherera mphatso ya mwana mu kachisi muja (1 Samuele 1:26). Yesu anati, “Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, khululukirani...” (Marko 11:25).

Kugwada popemphera inali njira imene imagwiritsidwa ntchito kuyambira kale maka panthawi yofuna kuonetsa kuti pakuchitika za dongosolo, ngakhale tikuwerenga za Daniele akupemphera nagwada pa mawondo ake katatu pa tsiku (Daniele 6:10). Solomoni anagwada pa kupatula kwa kachisi (1 Mafumu 8:54) ndipo Ezara anagwada pa mawondo ake pamene anasauka mumtima mwake pamaso pa Mulungu (Ezara 9:5). Davide anati, “Tiyeni, tipembedze tiwerame; tigwade pamaso pa Yehova, amene anatilenga” (Salmo 95:6). Pali nkhanu zambiri za oyera mtima a mu Chipangano Chatsopano akugwada pansu ndi kupemphera mu Machitidwe 21:5 ndipo Paulo anagwada kuti apemphere mu Machitidwe 20:36.

Mu Chipangano Chakale, pali nkhanu zambiri zimene zinalembedwa za anthu akupemphera atadziguwetsa pansu, mutu kugunda pansu maka panthawi ya masautso ndi mavuto ochuluka. Eliya mneneriyo anapemphera mutu wake uli pakati pa pawondo ake pamene mawondowo anagunda pansu (1 Mafumu 18:42). Anthu mu nthawi ya Ezara analambira mutu yawo itagunda pansu (Nehemiya 8:6). Sitingayiwale Mpulumutsi wathu amene “anagwa nkhope yake pansu napemphera” (Mateyu 26:39) m'munda wa Getsemane.

Malingana ndi malemba, pali njira zambiri zopempherera, ndipo munthu akhoza kumaganiza zokhazikika lamulo lokhala ndi njira imodzi yogwiritsa ntchito pamene tikupemphera. Nthawi yathu mu pemphero idzikhala yolemekezeka ndipo tidzilemekeza ndi kulambira Ambuye. Ndi mdalitso kumapemphera tikuyenda pansu, tikuyendetsa galimoto, komanso titagona pansu, koma chofunika kwambiri kwa mwana wa Mulungu ndi chakuti asachite ulesi ndi kuiwala tanthauzo, kakhaliidwe kamene anazolowera popembedza komanso kukhala chete popemphera.

Nkofunika kudziwa kuti Chipangano Chatsopano chimaphunzitsa kuti “amunawo apemphere pamalo ponse, ndi kukweza manja oyera” (1 Timoteo 2:8). Pali zitsanzo zambiri za mu mpingo wa Chipangano Chakale pamene anthuwo amapemphera atakweza manja awo poyamika kapena kunena zopempha kwa Ambuye Mulungu. Ngakhale kuti sitingakweze manja pa pemphero lililonse, ndikuona kuti ndi zogwirizana ndi Malemba ndipo tikuyenera kupitiriza mchitidwe panthawi zapadera za kuyamika kapena kumupempha Ambuye.

Kodi Baibulo limaphunzitsa chiyani za chilankhulo chosadziwika cha pemphero?

Nkoyenera kuti tidzitsogoleredwa ndi baibulo osati ndi zimene amazimva ndi kuchita iwo amene ali akhristu. Malemba saphunzitsa za chilankhulo chapadera cha pemphero pamene pempherolo lili mu chilankhulo chosadziwika ndiponso chakumwamba. Kodi tingaterenso chitsanzo chiti chabwino kuposa mwa Khristu mwiniwake. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera mosachulukitsa mau ndiponso momveka (Mateyu 6:9-13).

Nthawi zambiri anthu amagwiritsa ntchito mau a pa 1 Akorinto 14:14, “Pakuti ngati ndipemphera m'lilime, mzimu wanga upemphera, koma chidziwitso changa chikhala chosabala kanthu.” Dziwani kuti mau akuti chosadziwika anachita kuonjezedwa ndi otanthauzira ndipo mau akuti “lilime” amene ndi glossa, amatanthauza chinenero chachilendo. Sizitanthauza kumanena mau osamveka kapena kupemphera. Ngati munthu wina akupemphera mu chilankhulo chachilendo chimene wopempherayo akuchimvetsa, koma wina aliyense mu nyumbamo sakutolapo kanthu, kumvetsetsa kwa pempherolo kuli kosathandiza, ndi kosamangirira kwa iwo amene ali mu nyumbamo. Vesi 15 akulongosola bwino kuti: “Kuli chiyani tsono? Ndidzapemphera ndi mzimu, koma ndidzapempheranso ndi chidziwitso changa; ndidzaimba ndi mzimu, koma ndidzaimbanso ndi chidziwitso.”

Yesu anaphunzitsanso pa Mateyu 6:7 kuti tisamangobwere zabwereza mau monga m'mene amachitira akunja. Mapemphero athu tidziwapemphera ndi kumvetsetsa bwino komanso adzigwirizana ndi cholinga cha mtima wathu.

Ngati mukufuna kudziwa zambiri zokhudza mutu wa kulankhula kapena kupemphera m'malilime, chonde onani Gospel Truth, Kalata ya No. 9.

Kodi munthu apemphere motalika bwanji?

Palibe nthawi yeniyeni imene ili yolondola malingana ndi kutalika kwa pemphero. Kutalika kwa chitsanzo chimene Yesu anapereka mu pemphero la Ambuye ndi kosakwana mphindi imodzi. Yesu yemweyo anapempheranso usiku wonse komanso nthawi zina anapemphera nthawi zochepe. Zilipo nthawi zimene anthu samapemphera kwambiri, pamene ena, chifukwa chakuti ali pa msautso winawake, akhoza kupemphera kwa maora ochuluka mpaka kuiwala ntchito zina. M'mene ziliri zinthu zimapangitsa kuti pemphero likhale lotalika motani. Pamene wina wapsinjika kwambiri, pemphero lopemphera payekha likhoza kukhala lalitali komanso mwina kutenga usiku wonse. Nthawi zina zimatengera kukhala mu nyengo ya pemphero kuti ukalowe mu mzimu wa pemphero. Malingana ndi momwe zinthu zimakhallira, kupemphera kwa pagulu si nthawi yopemphera mapemphero aatali. Chimene chili chofunikira kwambiri ndi chakuti tilumikizane ndi Mulungu ndi kukhala ndi nthawi ya kumulambira ndiponso kumupempha. Anthu ambiri samavutika ndi kupemphera kwambiri!



KODI MUKUDZIWA?

Kuyambira kalekale, zipembedzo zochuluka zakhala zikugwiritsa ntchito mikanda yogwiritsa ntchito pa pemphero. Izi ndi monga chiHindu, chiBuddha, Chikhristu, Chisilamu, chiSikh ndi zipembedzo zina pofuna kubwereza mapemphero, ndi m'nthawi zachete. Mau a chingerezi akuti "bead" omwe amatanthauza "mkanda" amachokera ku chingerezi chakalekale chotchodwa "bede" chomwe chimatanthauza kuti pemphero. Ngakhale kuti chiyambi cha mauwa sichidziwika kwenikweni, kugwiritsa ntchito mikanda popemphera kukuoneka kuti kunali kuchitika kalekale pakati pa amitundu. Nthawi zoyamba zodziwika bwino zimene mikanda imagwiritsidwa ntchito popemphera ndi zaka zoposa mazana Khristu asanabadwe.

Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kuti asamapemphera mongobwereza mau. Pemphero ndiko kutsekula mtima wathu kwa Mulungu, osati kumangoloweza zinthu ndi kumangobwereza. Kugwiritsa ntchito mikanda yopempherera sikugwirizana ndi ziphunzitsa za Khristu.



**Mau a
Nyengo
Yake**

PEMPHERO LA YABEZI

Ndipo Yabezi anaitana kwa Mulungu wa Israele, ndi kuti, Mundidalitse ndithu, ndi kukulitsa malire anga; ndi dzanja lanu likhale ndi ine, nimundisunge, kuti choipa chisandivute. Ndipo Mulungu anafikitsa chopempha iye. —1 Mbiri 4:10

Pemphero la Yabezi limafunzulula mphamvu ndi kukoma komwe kuli m'pemphero lalifupi limene Mulungu analiyankha. Yabezi anayamba poitana Mulungu kuti amudalitse. Zoonadi, tifunikira madalitso a Mulungu pa miyoyo yathu, popeza kupanda lyeyo ife tili otayika ndi okhala kakasi. Mulungu ndi amene amatipatsa mpweya ndiponso mphatso iliyonse yabwino. Nkwabwino kotani kuyang'ana kwa Mulungu kuti atithandize ndi kutipatsa mphamvu kusiyana ndi kudalira kuthekera kwathu kapena kwa iwo amene atizungulira. Anthu akhoza kulephera koma Mulungu amakhalabe chimodzimodzi, popeza sasintha.

Kulitsani malire anga, Ambuye. Ndithandizeni kukula mu uzimu. Ndipatseni mphamvu ndi chisomo kuti ndizame mu zauzimu. Ikani pamoyo wanga mphamvu zogonjetsera ziphona zimene zili pamaso panga. Gwetsani makoma a malo otetezedwa m'moyo mwanga. Kuzani malo amene ndikhoza kufikira ku uzimu kuti potero ndigawe uthenga wanu wabwino kwa anthu amene ali kutali ndi ine.

Ambuye, kodi mukhoza kuika dzanja lanu pamoyo wanga? Pandekha sindingathe. Ndikudzichepetsa pampano wanu wachifumu ndipo ndi mtima wonse ndikupempha kuti mutambasule chifundo chanu. Ndikufuna chitsogozo ndi chisamaliro chanu. Ndikufuna nzeru ndi luntha lanu. Ndikufunitsitsa kudzodza kwanu ndi chivomerezo chanu.

Atate, muike kutali ndi ine choipa chilichonse kuti chisandiononge. Ndithandizeni kuti ndidzimvetsera Mzimu wanu. Ndiliba chilungamo pa ine ndekha ndipo ndikufuna kuti munditsekule maso anga akhunguwa kuti ndikhoza kuona.

Ndionetsereni misampha ya mdaniyo. Ndithandizeni kuti ndisalikonde dziko lapansi ndiponso kuti ndisanyengeke ndi chipembedzo chonyenga. Njira yanu ndiyo njira yokhayo imene imakafika kumwamba, ndipo ndikukupemphani kuti munditeteze ndi kutchinjiriza moyo wanga kuti potero ndisakuchimwiren.

Mulungu anamva pempherolo, ndipo mwachidule, "Mulungu anamupatsa chimene iye anapempha." Mulungunso atichitira ife lero zimenezi, muyamiken! Limbani mtima, mwana wa Mulungu mnzangawe ndipo ti yeni tipirirebe kupemphera! ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Mapemphero otchuka

PEMPHERO LA AMBUYE

Mateyu 6:9-13

PEMPHERO LA YONA LA CHIPULUMUTSO

Yona 2:2-9

PEMPHERO LA HEZEKIYA LA MACHIRITSO

2 Mafumu 20:1-5

PEMPHERO LA SOLOMONI LA KUDZIPEREKA

1 Mafumu 8:22-53

YOSWA MKULU WA NSEMBE

Nehemiya 9:5-38

PEMPHERO LA YABEZI

1 Mbiri 4:10